


# Pempero La Mtendere



Chichewa

## Maranatha

## Pempero La Mtendere

Kwaganizidwa kuti pempherori tipemphere pang'onopang'ono tili pamalo achete.

*Ndabwela mwa ine ndekha  
M'mene ndilili  
Mu nthawi ino  
Zokumva zanga,nkhawa zanga  
Chimwemwe changa,kukhumudwa kwanga.  
Mumandiona monga m'mene ndilili  
Mukundidziwa bwinobwino  
Mumaona chonse chimene ndili  
ndi chimene ndinali*

*Zonse zimene ndadutsamo m' moyo mwanga zili poyera  
pamaso panu.  
Zithunzi zonse zomwe ndaona,  
zimene ndagwira ,zimene ndamva  
liu lililonse limene ndalankhula kapena kumva  
liu lililonse ndi lingaliro lililonse  
maganizo onse amene akhazikika mumtima mwanga  
Ndiodziwika pamaso panu.  
Mumandidziwa kuposa mzanga wa pa mtima  
Mumandidziwa kuposa m'mene ndimadzidziwira ndekha  
Mumadziwa  
Ndipo ndichifukwa cha chimene ndili  
Osawelengera chimene ndili- mumandikonda.  
Ndine wa mtengo wache kwa inu  
Mumandikonda mu zonse  
Palibe chinthu kapena munthu amene angandichotse pa  
chikondi chanu  
Palibe chinthu kapena munthu amene adzandilekanitse  
pa chikondi chanu ndi nkupezeka kwanu*

*Mumandidziwa pa nthawi imene mumandilenga  
Munthawi imeneyo munandikonda  
Mumandidziwa ndikundikonda ndili mimba mwa mayi  
wanga  
Chikhalidwe changa chinadziwika pamaso panu  
Mumanditchula ndi dzina langa  
Mumandifungatira manja mwanu  
Mumandikumbatira ine*

*Munapumila mpweya mwa ine  
Munandipatsa moyo wanu ndi chikondi chanu.  
Munandiyang'anira pa umwana wanga  
Mwandiyang'anira kuyambira ndili wakhanda  
Mumapezeka nthawi zonse malo ena aliwonse  
Anzanga osewera nao osawoneka,anzanga  
akusukulu,akuntchito  
Mlendo wosaoneka pa nthawi ya chakudya  
Munagawana nane muzonse ndakumana nazo  
Munandiyang'anira mwakachetechete  
Ngakhale mu maola ataliatali ausiku  
Munatengapo gawo pa ulendo ulionse  
Munayenda nane  
Munalinane pakuyamba ulendo ulionse  
Munali nzanga pa ulendo.  
Popanda inu nditaya njira yanga  
Ulendo wanga ukhala wopanda cholinga.  
Ndinalefuka pa njira  
Koma inu ndinu Alepha ndi Omega  
Ndinu njira yanga  
Ndinu njira, njira ya moyo*

*Ndiye Ambuye ndipeleka moyo wanga pamaso panu  
Dzulo langa lonse,  
lero langa Ndi mawa langa  
Ndikutamandani ndi kukuthokozani chifukwa  
chakupezeka kwanu  
Moyo wanga  
Ndikukwezeka mothokoza zabwino zonse ndi chimwemwe  
chonse.  
Tsopano ndikupereka zondikhumudwitsa  
zonse,zopweteka ndi kukandwa kwanga  
Ndapeleka kwa inu zinthu zonse zondipatsa manyazi  
Zomwe ndanena,ndinachita ndi zomwe ndaganiza  
Zonse zimene zakukhumudwitsani ndi kukhumudwitsanso  
ena.  
Ambuye ndikhuthulileni madzi oyeretsa amitsinje  
yamoyo,m'moyo wanga wonse.  
Pangani chipululu cha moyo wanga chitumphuke ndi  
moyo  
Nditsitsimutseni ndipangeni watsopano  
  
Ambuye ndipumileni kwatsopano  
Ndipo ndidzalandila moyo wanu.  
Ambuye tambasulani dzanja mundikhuze*

Ndipo ndidzalandira machiritso anu.  
Khuthulani zonyansa zonse mwa ine.  
Nthawi ino Ambuye chotsani zondiononga zonse,  
mayesero onse,malingaliro ndi zikhumbo zonse zoipa  
chotsani zondilemetsa  
Chotsani mantha onse obisika

Ndithandizeni kudziwa  
Kuti chikondi chanu cholungama chimachotsa  
mantha onse

Ndibweletseni tsopano m' malo ozama achete  
akupezeka kwanu  
Ndikupeleka thupi langa ndipo ndikupempha kuti likhale  
malo anu okhalamo  
Nthawi ino lolani kuti moyo wanga onse  
ukhale pa mtendere  
Lolani kupuma kwa mtima wanga kukhale mu umodzi ndi  
kupuma kwa mtima wanu  
Lolani gawo lililonse la thupi langa lidzadzidwe ndi  
Mzimu wanu  
Tengani mtsempha ulionse wa magazi anga  
Tengani gawo lililonse la zidziwitso muthupi langa,  
Tengani mulofu uliwonse ndi chiwalo chilichonse  
Ndizadzeni tsopano ndi bata lanu  
Komanso ndi kupezeka kwanu kwenikweni  
kwa moyo wanu

Ndithandizeni kupempha tsopano ngakhale  
popanda mau  
Ndithandizeni kupempha nkupuma kwanga  
Ndipumile nkati mphweya wa chikondi ndi  
mtendere wanu  
Ndipumile kunja ululu ndi kukhumudwa kwanga  
Ndipumile nkati kutsukidwa ndi kukhululukidwa  
Ndipumile kunja zopsinja ndi zonyansa  
Kotero pakupuma kwa thupi langa ndi moyo wanga  
zikhale pa mtendere ndi Inu  
Nchiyanjano ndi Inu  
Momasuka ndi Inu  
Ndikhale chete ndikudziwa kuti ndinu Mulungu.  
Ndikhale chete ndikudziwa kuti ndinu Ambuye  
opereka machilitso

Ndithandizeni kumva mau anu abata Ambuye yesu  
Ndimve mau anu akuti- mtendere khala chete  
Mphepo zanga zonse zitonthole pamene ndabvomereza  
kupezeka kwanu kwenekweni

Pamene ndikugwada pamaso panu  
Ndikupereka mtima wanga ndi nzeru zanga zonse  
Malingaliro anga onse ozama amene ali obisika kwa ine  
Ndikupereka kwa Inu bata langa  
Koma ndikuperekanso kwa Inu zondipsinja,Mtanda  
komanso mafunde amoyo wanga  
Malingaliro anga akulephera komanso kukanidwa

Ndikukupatsani ubwenzi uliwonse  
Nyengo iliyonse ya moyo wanga  
Kusadzigwira kwanga  
Kulankhula mokhadzula pamene ndakondwa komanso  
pamene ndakwiya  
Nyengo zakukondwa komanso zokhumudwa

Ambuye ndipeleka nzeru zanga  
Ndaika pamaso panu maganizo onse opanda pache  
Ndipeleka kwa inu kufunafuna ndikuyesetsa kwanga  
Kugwiritsitsa choona

Ndipereka kusadziwa ndi kusokonekera kwanga  
Ndipereka mafunso ndi kukaika  
Ndikuvomereza inu kukhala choona  
Choona chenicheni  
Choona chonse nkuyera kwake  
Choona chindimasula, mthupi,malingaliro ndi mumzimu.  
Kumasuka ku ukapolo ulionse  
Kumasuka ku bodza ndi chinyengo cha dziko lapansi  
Kumasuka ku mtima wodzikonda,kunyada ndi dyera.  
Ambuye dulani nsinga zondibwezera m'mbuyo  
Tsegulani chitseko chondiyika mundende,  
Kuti ndidutse mu mdima wa dziko lino- dziko langa  
ndipo ndiyende mu kuwala koposa ,kuwala kwa  
kupezeka kwanu.  
Atate tsopano ndimve kuwala kwa chikondi chanu pa ine  
Ndimve kukoma kwa chikondi cha bambo  
pa ine mwana wanu.  
Kukukhulupirirani,kukudalirani,kukukondani  
Ndithandizeni kudziwa zimene chimwemwe changa  
chimabweretsa pa Inu  
Ndipatseni chisomo mu zofooka kuti ndifuule Abba Atate.

Ndithandizeni kudziwa kuti paine pali manja ondigwira  
mpaka muyaya.  
Ambuye Yesu khalani Mbuye wa moyo wanga,  
Mbuye wa malingaliro ndi zokhumba zanga,  
Mbuye wa chikumbuntima.ndi chiyembekezo changa.  
Ndikuvomera ulamuliro wanu pa zonse zimene  
ndinali,ndili ndiponse ndidzakhale.

Ndikupeleka ulemu kwa Inu  
pamene ndikuonani pa mtanda wanu

Munakhomedwa ndi misomali yankhanza  
Ndikuona manja anu otambasuka kufuna ku kumbatira  
dziko lonse  
Kufuna kukumbatira ine  
Kufuna kukonda  
Kufuna kukhululuka  
Kufuna kundipanga wathunthu

Nditamanda inu kuti munandifera  
Ndithandizeni kuzindikira kuti chikondi chanu  
pa ine chinali chachikulu,  
Inenso ndiyenera kumadzikonda ndekha  
Ndizindikire kuti ndine wamtengo wake kwa Inu

A Mzimu Oyera, chiyambi cha choona chonse,opereka  
mphamvu  
bwerani pa ine tsopano,  
Modekha ngati nkhunda  
Kapena ngati malilime amoto woyaka  
Modekha ngati kamphepo ka mchilimwe  
Kapenanso ngati mphepo yamphamvu yobangula,  
Bwerani ndikukhala pa ine.  
Ndithe kuchita zimene zinali zosatheka poyamba

Osayenerera ine,Mzimu oyera wa Mulungu wa moyo  
Ndipatseni mthatso zimene ndingagwiritse ntchito  
zokupatsani ulemu ndi ulemelero  
Kuti ndionetse chipatso chanu  
Ngakhale ku moyo wanga.

Ulemelero ukhale kwa Inu Atate  
Ulemelero ukhale kwa Inu Ambuye Yesu  
Ulemelero ukhale kwa Inu Mzimu oyera.  
Amen